# Makalasi opanda Mipanda

FUFUZANI - ZINDIKIRANI - PHUNZIRANI - KONDANANI

## Lowani nafe paulendo wosangalatsa wopezeka mudziko lopatsa chidwi la mileme!

Moni, mwalandilidwa kuMakalasi opanda Mipanda - ulendo wanu wosangalatsa wodziwa m'miyoyo yachinsinsi ya mileme! Dzina langa ndine Spike ndipo ndine mleme wopanda mchira. Ndasangalala kukumana ndi munthu wokonda mileme. Ndine wokondwa kukuuzani zambiri za mileme, kusangalala limodzi, ndikukudziwitsani kwa anzanga apamtima!

Anzathu a Bats without Borders akhala akukondwelela kugwira ntchito nane kuti apange maphunziro 8 osangalatsa kwa inu. Kodi mukufuna kudziwa zomwe muphunzira pamaphunzirowa?



### Nawu mndandanda wazomwe zikubwera!

Phunziro 1

**Kodi mileme ndi chiyani?**

Dziwani zambiri za mileme ndi zomwe zimawapangitsa kukhala apadera kwambiri.

Phunziro 2

**Kusiyanasiyana kwa mileme**

Phunzirani za mitundu yosiyanasiyana ya mileme, ndi kusiyana kwake konse.

Phunziro 3

**Kodi mileme imakhala kuti?**

Dziwani komwe kumakhala mileme yosiyanasiyana (ndi malo ena osazolowereka omwe amawatcha kwawo!).

Phunziro 4

**Kodi mileme imadya chiyani?**

Onani zakudya zomwe mileme imakonda (kodi palinso yomwe mumakonda?)

Phunziro 5

## Ana a mileme

Dziwani za makanda a mileme, ndi zomwe amatchedwa!

Phunziro 6

## Luso lowuluka modabwitsa

Ndikubetchera mumafuna mukuwuluka? Kuuluka ndi chifukwa china chimodzi mileme ili yosangalatsa




Phunziro 7

## Chiwopsezo ku mileme

Onani zifukwa zomwe mileme ili pachiwopsezo.

Phunziro 8

## Zomwe mungachite kuti muthandizire mileme!

Pezani njira zomwe mungatengere nawo mbali ndikuthandizira mileme.



Pa maphunziro 8 awa, tikuwuzani zinthu zambiri zabwino za mileme, kuti mukhale ndichithunzithunzi pang'ono pa zomwe zikubwera nazi mfundo zisanu zosangalatsa zokhudza mileme:

Timatha kuwuluka!
Timapezeka pafupifupi dziko lonse lapansi!
Ena aife timagwiritsa ntchito luso yapadera yotchedwa ekolokeshoni kuti tisatile njira yomwe tikupita (ganizirani ngati kupanga chinthunzi ndi mawu).
Takhalapo kwa nthawi yayitali!
Ena aife timakonda kukhala mozondoka (monga ine)!

### Mleme ndi anthu amafanana mwanjira zina...

"Ndakhala ndikudziŵa zambiri zokhudza anthu, ndipo eah ndinu wodabwitsadi! Ndinasangalala kumva kuti mumadyetsa ana anu mkaka, ndi chimodzi mwa zinthu zomwe TIKUFANA. Mileme ndi anthu onse ndi nyama zoyamwitsa."

# Kodi mileme ndi anthu amasiyana bwanji? Kodi mukufuna kudziwa chifukwa chomwe ndimaona kuti anthu ndi odabwitsa?



Ndamva zinthu zodabwitsa zokhudza anthu. Ndizoonadi kuti anthu....





...amadzuka dzuwa likatuluka ndipo kugona kukada?
(ndiku kubwerera kutsogolo kwa ine!)

... sungathe kuwuluka?!









Amayendela mapazi, mitu yawo ili mmwamba, mmalo molendewera ndi mapazi awo, mitu ili yawo pansi?

... amawona ndi maso awo ndipo sangathe kupanga ekolokeshoni?

... amakhoza kuimba ndi kuyankhula koma amangopanga manotsi otsika ndipo sangathe kupanga kapena kumva mawu okweza, omwe mileme ife timatha kupanga?



Ndili ndi zambiri zoti ndiphunzire za anthu, koma eah moyo wanu umawoneka wachilendo komanso wosiyana kwambiri ndi wanga!



# Kumanani ndi abwenzi anga!

Pa maphunziro athu, anzanga ena a mileme adzabwera kudzatithandiza.
Hei azizanga osangalatsa, mukufuna kudzidziwitsa nokha?!



Moni, ndine Zeke (ndi mawu okweza kwambiri). Ndikhoza kukhala wamng'ono koma ndili ndi mawu okweza kwambiri kuposa mileme yonse ku Southern Africa (pafupifupi 210 kHz). Mawu anga ndiwokwera mowirikiza kakhumi kuposa momwe munthu aliyense angamvele.
Ndine mleme wam'makutu amfupi wa Percival. Ndimatchedwa dzina la Katswiri wina dzina lake Percival, ndili ndi makutu aafupi (koma okongola) ndipo ndili ndi tinthu ting'onoting'ono titatu patsamba langa lamphuno lomwe limawoneka ngati mkondo wosongoka katatu.



Moni kumeneko! Ndine Avnaya, ndine mleme wamapiko achikasu. Ndikukhulupirira kuti mumaganiza kuti mileme yonse ndi yokuda. Osati ine, ndine wamkulu, wowala komanso wokongola!



Moni! Ndine Logan, mleme wa makutu atali waku Botswana. Ndimakhala nditagona pansi pa phiko la amayi anga (Bongi) ndikumwa mkaka. Ndilibe ubweya wambiri panobe koma izi zikukula. Ndikangokwana masabata anayi ndidzayamba kuphunzira kuuluka kenako ndiyamba kugwira tizilombo. Ndikukhulupirira kuti ndidzakhala ndikuwuluka bwino ndikadzakwana masabata asanu ndi limodzi ndipo sindidzafunikiranso mkaka.






# Ntchito yosangalatsa kwa inu:

Kodi mukuwona kusiyana kwake?

Pali kusiyana 5 pakati pa zithunzi ziwiri zomwe zili pansipa, mungapeze kusiyana kwake?





